Uthenga Wabwino wa Yesu

Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu

Kubadwa Kwake Kwa Yesu – Phunziro 1, Mateyu 1-2

By Christy Akins Brawner

“Motero mibadwo yonse kuyambira pa Abrahamu kufikira kwa Davide ndiyo mibadwo khumi ndi inayi; ndi kuyambira pa Davide kufikira pa kutengedwa kunka ku Babulo mibadwo khumi ndi inayi; ndi kuyambira pa kutengedwa kunka ku Babulo kufikira kwa Khristu mibadwo khumi ndi inayi.” Mateyu 1:17

Maria, mzimayi wa pfuko la Chiyuda, anapezeka ali ndi pakati wopanda kukomana ndi mwamuna. Anapezeka ndi pakati pa Mzimu Woyera. Bwenzi lake monga munthu wachilungamo sanafune kumnyazitsa iye, anafuna kuthetsa ubwenzi wake mwa chinsinsi. Koma usiku umene anali kuganizira chomwecho, mngelo wa Ambuye anamuonekera iye m’kulota nanena, “Yosefe, mwana wa Davide, usaope kutenga mkazi wako Maria, pakati pamene ali napopa ndi pa Mzimu Woyera. Ndipo iye adzalandira mwana wa mwamuna, ndipo udzamutcha dzina lake “Yesu” popeza Iye adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo. Maria ndi mkazi mmene mneneri Yesaya analankhula m’Chipangano Chakale ponena, “Taonani, namwali adzakhala ndi mwana, nadzakhala ndi mwana wa mwamuna, ndipo adzamutcha dzina lake Emanuele, lithantauza ‘Mulungu ali nafe.’”

Yosefe anauka ku maloto ake ndi kumvera mngelo. Iye anakwatira Maria, koma sanakhalire limodzi naye kufikira kubadwa kwa mwana. Ndipo Yosefe anamutcha mwanayo dzina lake Yesu, monga mwa malangizo amene analandira kwa mngelo. Tsopano Yesu anabadwira mu mzinda wa Betelehemu mu dera la Yudeya m’dziko la Israeli, ndipo mfumu ya Yudeya nthawi imeneyo dzina lake linali Herode.

Kunali anzeru amene anachokera ku Yudeya motsogololedwa ndi nyenyezi. Kupyolera mu zimene anali kuphunzira, nyenyezi imeneyi inaonetsera kuti mfumu yolonjezedwa wabadwira ku Yudeya. Sanadziwe kwenikweni mwanayo adzamupeza kuti. Poyamba anafika kwa mfumu Herode, mfumu ya m’dera la Yudeya ndi kumfunsa iye, “Kodi mfumu yatsopano ya Ayuda yabadwira kuti?”

Mfumu Herode anakhumudwa ndi mbiri imeneyo naitanitsa msonkhano wa m’tseri kuitanitsa alangizi onse a chipembedzo ndi ansembe. Anawafunsa anthu amenewo, kuti molingana ndi ulosi wa Chiyuda, “Kodi mfumu ya Ayuda yolonjezedwa idzabadwira kuti?” Alangizi ndi ansembe amenewa anamfotokozera Herode kuti kulingana ndi malembo, mwana wolonjezedwa adzayenera kubadwira ku Betelehemu. Herode anapita kwa anthu aja anzeru nawafunsa iwo kuti, “Kodi nthawi ndi yiti imene munaona nyenyezi? Anafunsa cholinga choti adziwe zaka zake zenizeni.

Herode anawauza anzeruwo a mzinda umene anali kuyembekezera kuti adzabadwire. Komanso ananena, “Pitani mukafufuze khandalo, ndipo nthawi imene mumpeze iye, bwerani kwa ine, kuti inenso ndipite ndi kamulambirenso.”

Anzeru aja anachoka napitiriza ulendo kulondola nyenyezi ku Betelehemu. Nyenyezi imene inawatsogolera inaonekera patsogolo ndipo inaima pamwamba pa nyumba pamene mwanayo anabadwira. Iwo analowa m’nyumba, ndipo ataona mwanayo ndi Maria mayi wake, anagwada pansi namulambira Iye. Iwo anaperekanso mphatso za mtengo wapatali: golide, lubano ndi mure.

Tsono anzeru aja anachoka ku malo kumeneko kubwerera kwawo. Koma asanachoke kubwerera, analota maloto owachenjeza kuti asabwererenso kwa Herode kuti amudziwitse m’mene angathe kumpezera mwanayo. Choncho anabwerera kwawo podzera njira yina.

Atangonyamuka, Yosefe analotanso loto lina. M’kulota kwake, anachenjezedwa ndi Mulungu kuti Herode adzafika kwa mwanayo ndipo ayenera kuthawira ku Ejipito. Choncho usiku womwewo, iye anadzuka ndi banja lake nathawa nthawi yomweyo. Anakhala ku Ejipito kufikira Herode atamwalira. Izi zinakwaniritsa za ulosi wa mneneri Hoseya m’mene ananena, “Ndinaitana Mwana wanga atuluke ku Ejipito.”

Herode anakhwiya kwambiri atazindikira kuti anapusitsidwa ndi anzeru aja. Iye analamulira kuti ana onse amuna osachepera zaka ziwiri ayenera kuphedwa. Inali nthawi yovuta ya kupha ana onse ang’ono ku Betelehemu ndi ena ozungulira. Mneneri Yeremiya analosera zimenezi.

Atamwalira Herode, mngelo anaonekeranso kwa Yosefe ndi kumuuza kuti ayenera kubwerera ku Israeli. Yosefe ngakhalebe anali ndi mantha chifukwa choti mwana wake wa Herode analowa ufumu ku Yudeya, tsono iye anasuntha ndi banja lake nakhala kwa abale ake ku dera la mzinda wa Nazarete. Yesu anakhala komweko nthawi ya unyamata wake. Izi zinakwaniritsa ulosi wonena, “Adzatchedwa Mnazarete.”

MAFUNSO

1. Maria ndi yani?
2. Mngelo anaonekera kwa yani? Ananena kuti Mwana adzachedwa dzina lotani?
3. Ndi chifukwa chiyani anzeru a kummawa anabwera ku Yudeya?
4. Ndi chifukwa chiyani Herode anafuna kukaona Yesu?
5. Anzeru anazindikira bwanji kuti anayenera kubwerera njira yina poopa Herode?
6. Herode anakonza njira yanji kuti aphe mfumu ya Ayuda?
7. Yosefe anazindikira bwanji kuti ayenera kuthawa ndi mwanayo ndi kupita ku Ejipito?
8. Yosefe anazindikira bwanji nthawi imene anayenera kubwereranso?
9. Ndi chifukwa chiyani Yosefe anatenga banja lake kukhala nalo ku Galileya m’dziko la Yudeya?
10. Kodi ndi mzinda wuti umene Yesu anakhala ali mwana?

ZOONA ZA UZIMU

1. <u>Mulungu ndi wokhulupirika ndipo amasunga malonjezano ake nthawi zonse</u>. Kuyambira nthawi ya chilengedwe cha anthu awiri oyamba, Mulungu analonjeza kuti adzatumiza Mpulumutsi pa dziko lino. Mu zaka zambiri Iye anabwereza malonjezo ake nthawi zambiri kwa anthu ambiri ndi ndondomeko zimene kubwera kwake kudzakhala kotani. Yesu anabwera pansi pano monga momwe malembo analosera. Kumbukirani nthano imodzi ya uneneri umodzi umene ulosi wake unakwaniritsidwa kupyolera nthawi ya kubadwa kwa Yesu.

*Mulungu ali wokhulupirika kwa ife mu njira yomweyo. M’Mawu a Mulungu muli malonjezo ofunikira ambiri amene Mulungu wapanga za Cholinga Chake kwa ife. Iye adzakwaniritsa malonjezo ndi ulosi. Ndi chofunika kuti tiwerenga malembo ndi kufufuza malonjezo a Mulungu ku miyoyo yathu.

2. <u>Baibulo ndilo Mawu a Mulungu, ndi chilichonse chili m’meneno ndi choona</u>. Mulungu analankhula kupyolera mwa aneneri kufotokozera za kubadwa ndi moyo wake wa Yesu zaka zikwi izi zisanachitike. Zilizonse zinachitika chimodzimodzi monga zinalosedwa.

3. <u>Mulungu ndiye woyendetsa zinthu zonse</u>. Iye angachite zinthu zina zichitike modabwitsa. Zilipo zinthu zodabwitsa mu nthano imeneyi zimene zinachitika. Chimodzi mwa icho ndi chiyani?

4. <u>Mulungu akhoza, ndiponso amatha kulumikizana ndi anthu</u>. Ena amakhulupirira kuti Mulungu analenga dziko koma sasamalira zimene zikuchitika pano. Ndi mu njira yiti kuti Mulungu alumikizana ndi anthu mu nthano imeneyi? Mulungu amalumikizana ndi ife lero. Ife tidzaphunzira m’mene ife tingakhalire ndi chiyanjano chenicheni ndi Mulungu.

5. <u>Mulungu amadziwa chilichonse chimene chidzachitika</u>. Koma nthawi zina, mu nzeru yake, Iye amalola zinthu zovuta kuchitika. Herode anafuna kupha Mfumu Yolonjezedwa chifukwa iye anazindikira kuti Yesu anali choletsa. Mulungu anazindikira za mfumu yoipayo zimene zinali mu mtima mwake. Iye anadziwa kuti adzapha ana mazana ambiri. Chifukwa cha kusamvera ndi kuukira mu mtima mwake mwa Herode, zoopsya zazikulu zinachitika. Lero nthawi zambiri, zoopsya zimachitika chifukwa cha kusamvera ndi kuukira m’miyoyo yathu. Kodi mukudziwa chitsanzo cha masiku ano cha wina amene amakhala ndi vuto chifukwa cha kuipa kwa anthu ena?

6. Palibe munthu amene angalimbane ndi Mulungu ndi kupambana Iye. Herode analephera kupha Mwana Wolonjezedwa. Chinthu cholakwa chimodzi chokha chimene anakwaniritsa ndi kukonza chinali choopsya pa miyoyo ya mabanja ambiri. Lero nthawi zambiri ife timayesa kuononga malamulo a Mulungu ndi chifuniro chake. Izi zimabweretsa zoopsya kwa ife, ndiponso anthu otizungulira amavutisidwanso. Kodi mungaganizire m'moyo mwanu nthawi imene munachita choipa ndi kubweretsa vuto mkati mwa moyo wanu? Mukhoza kuganizira nthawi yina inuyo munamva kuwawa chifukwa cha kuuikira kwa munthu wina?

7. Ansembe ndi atsogoleri a chipembedzo anazindikira malembo okhuza za Mfumu Yolonjezedwa koma sanafune kupita kukomana ndi Yesu. Kodi nkutheka kukhala wa chipembedzo, kudziwa zambiri za Mawu a Mulungu, kudziwa zambiri za Yesu Khristu, Koma kusamdziwa Iye kwenikweni mkati mwa moyo wanu?

8. Yesu ndiye "Mulungu alinafe, " kapena "Emanuele." Mngelo analankhula mawu awa kwa Yosefe, ndipo analembedwa m'Malembo ndi mneneri Yesaya. Anthu ambiri amanena kuti Yesu anali meneri. Ena amanena kuti Iye anali mngelo kapena munthu wabwino. Koma Mawu a Mulungu amatiphunzitsa ife kuti Iye anali "Mulungu ali nafe."

Masiku akubwera tidzafufuza za Yesu Khristu ndi Uthenga Wabwino umene anatibweretsera pa dziko lino.

Uthenga Wabwino wa Yesu;
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kubatizidwa Kwake Kwa Yesu – Phunziro 2, Mateyu 3-4

"Tembenukani mtima; chifukwa Ufumu wa Kumwamba wayandikira" Mateyu 3:2

KUBWEREZA

1. Mayi wake wa Yesu anali yani?
2. Chozizwa chimodzi cha kubadwa kwake kwa Yesu ndi chakuti anabadwa mwa mkazi wotani?
3. Chipangano Chakale zinena zinthu zambiri za kubadwa kwake kwa Yesu. Chinthu chimodzi cha izi ndi kuti Iye adzatchedwa, "Imanuele." Kutanthauza kwake ndi chiyani?
4. Herode anayesa kumupha Yesu. Herode anali munthu wa ntchito yotani? Kodi anachita chiyani ndi ana onse osachepera zaka ziwiri amene anakhala kufupi ndi Betelehemu?
5. Anzeru a kum'mawa amene anapita kukaona Yesu anatsatira chiyani? Atamuona Yesu, anadzera m'njira yina pobwerera chifukwa Mulungu anawachenjeza kuti Herode anafuna kuchita chiyani ndi Yesu? Kodi Mulungu anawachenjeza iwo bwanji?
6. Mulungu anamuonetsera Yosefe bwanji kuti ayenera kuchoka mkati mwa usiku ndi banja lake kupita ku Ejipito? Kodi ndi yani amene anawathamangira?
7. Kunali mwa njira yotani kuti Yosefe anadziwa kuti kunali kwabwino kubwerera ku Israeli? Iye sanabwerere ku Betelehemu, koma anatenga banja lake nafika ku mzinda kuti?
8. Monga momwe Iye wachita mu mbiri yonse, kodi lero Mulungu akusungabe chiyani?
9. Ngakhale muli zinthu zoipitsitsa zambiri, kodi Mulungu amadziwa zonse m'mitima yathu?
10. Nkotheka kukhala munthu wopembedza, mwina kudziwa zambiri za m'Mawu a Mulungu koma m'mtima kusadziwa ndani?

Awa ndi mawu amene analalikidwa ndi munthu wopezeka m'chipululu cha Yudeya. Munthu ameneyu anavala zovala za ubweya wa ngamila ndi lamba la chikopa m'chiuno chake. Anakhala pa kudya dzombe ndi uchi wa kutchire. Dzina lake linali Yohane Mbatizi.

Anthu ambiri ochokera mbali zonse zozungulira mu mtsinje wa Yordani anapita ku chipululu kukamva uthenga wake. Atamva uthenga wake, ambiri anabatizidwa mu mtsinje wa Yorodani pambuyo pakuulula machimo awo. Ambiri mwa atsogoleri a chipembedzo otchedwa Asaduki ndi Afarisi anabwera kuona zimene zinachitika ku chipululuko. Nthawi imene Yohane anawaona, anawatchula iwo ana a njoka, kunena kuti sanachite mantha ndi Mulungu chifukwa anadziganizira mwa iwo okha kuti anali a chipembedzo ndi anthu abwino kuti sayenera kulapa machimo awo.

Nthawi yomwe Yohane analalikira Yesu anafika kwa iye napempha kuti amubatize Iye. Yohane poyamba sanafune chifukwa anaganizira kuti iye sanali woyenera kubatiza Yesu. Koma Yesu anamuumiriza ndipo onse awiriwo analowa mu mtsinje wa Yordani. Nthawi imene Yesu anatuluka m'madzi, Mzimu Woyera anatera pa Iye kuchokera kumwamba monga ngati nkhunda. Komanso mawu akulu anachokera kumwamba akunena, "Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa. Mwa Iyeyu ndikondwera."

Pambuyo pake pa izi Mzimu Woyera anatenga Iye kupita ku chipululu kukayesedwa ndi Satana. Iye anasala chakudya kukwanira masiku makumi anayi usana ndi usiku. Pambuyo pa masiku makumi anayiwa anali ndi njala. Inali nthawi imeneyi Satana anafika kukamuyesa Yesu.

Mawu a Mulungu afotokozera mayesero atatu amene Yesu anayesedwa nawo m'chipululu. Mu yesero loyamba Satana anayesa kuuza Yesu kuti asandutse miyala kukhala mkate, kuonetsa kuti zidzamutsimikizira kuti Iye anali Mulungu. Yesu anamuyankha iye pa kugwiritsa ntchito Mawu olembedwa a Mulungu. Kachiwiri Satana anamtenga Yesu kukamuimitsa Iye pamwamba pa kachisi ndi kumfunsa Iye kuti alumphe pamwambapo kudzitsimikizira kuti anali Mulungu. Koma Yesu anamuyankha iye kachiwiri pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Potsiriza Satana anamutenga Iye kukafika pamwamba pa phiri nanena, "Zinthu zonsezi ndidzakupatsani ngati iwe mutangogwada ine." Yesu anamuyankaha ndi kunena kuti, "Udzapembedza Mulungu Mbuye wako ndi Iye yekhayo udzamtumikira." Ndi mawu amenewo Satana anamusiya, ndipo angelo anabwera kudzamtumikira Iye.

Pambuyo pa kutsika kuchokera ku chipululu, Yesu anamva kuti Yohane Mbatizi anagwidwa naikidwa m'ndende. Yesu tsono anapita ku Galileya, ku dera la kumpoto kwa Yudeya, nasiya ku mzinda kumene Iye anakulera, Nazarete, napita ku Kapernao . Izi zinali kukwaniritsa zimene zinanenedwa ndi mneneri Yesaya m'mene ananena, "Ku dera la Zebuloni ndi ku malo otchedwa Nafutali, mu mphepete mwa nyanja, kupyola Yordani, Galileya ku pfuko la amitundu: Anthu amene ali mu mdima aona kuwala kwakukulu, ndi iwo amene akhala m'dera lonse la mthunzi wa imfa wa mdima walowa."

Mawu a Mulungu amatiuza ife kuti m'mzinda muno Yesu anayamba ntchito yake poyera kwa anthu. Uthenga amene analalikira unali, "Lapani, Ufumu wa Mulungu uli pafupi."

MAFUNSO

1. Fotokozani za munthu wotchedwa Yohane Mbatizi.
2. Uthenga wake wa Yohane unali chiyani?
3. Yohane ankachita chiyani ndi iwo amene analapa machimo awo?
4. Ndi chifukwa chiyani Yohane sanafune kubatiza Yesu?
5. Yesu anabatizidwa motani?
6. Chinachitika chiyani Yesu atatuluka m'madzi?
7. Ndi chifukwa chiyani Yesu anapita ku chipululu?
8. Yesu anachita chiyani masiku makumi anayi usana ndi usiku?
9. Ntchito imodzi ya kuyesa kwa Satana inali chiyani?
10. Atangotha kuyesedwa, ndani anabwera kumtumikira Yesu?
11. Yesu anapita kuti nthawi imene anamva za kuikidwa m'ndende kwa Yohane Mbatizi?
12. Uthenga wake wa Yesu unali chiyani? Ndani analalikiranso uthenga womwewo?

ZOONA ZA UZIMU

1. Uthenga wa Yohane Mbatizi ndi uthenga wa Yesu unali wofanana. "Lapani chifukwa Ufumu wa Mulungu uli pafupi."
   *****<u>Kulapa kumatanthauza kutembenukira ku tchimo m'moyo mwanu. Lithanthauza kuti kudzipereka kwa tunthu kwa moyo wanu kwa Yesu Khristu</u>.
   *<u>Tchimo ndi kusamvera Mulungu ndi malamulo ake</u>.
   *****Kodi kulapa kungakhale kovuta kwa munthu kuchitapo? Kodi liwuli lithanthauza chiyani kwa inu? *Kambiranani ndi anthu amene ali m'gulu mwanu; lolani munthu aliyense kukhala ndi mwayi kuti afotokozere maganizo ake*.

2. Atsogoleri a chipembedzo anaganiza kuti iwo sanayenere kulapa machimo awo chifukwa cha chipembedzo chawo. Anaganiza kuti anali wabwino wokwanira. Yohane anatchula anthu amenewo "ana a njoka." Kodi alipo ena padziko lapansi amene ali a chipembedzo kapena abwino koposa kuti sayenera kulapa machimo ake?

* Mawu a Mulungu anena pa Aroma 3:23 kuti, "Pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemerero wa Mulungu."
*Kodi alipo wina padziko lapansi amene alibe tchimo m'moyo mwake? Kodi alipo wina amene amamvera Mulungu nthawi zonse kapena amakhala wabwino monga Iye nthawi zonse? Mawu a Mulungu anena kuti, "Ayi." Kodi mukuvomerezana nalo Mawu a Mulungu kuti tonse tili ndi machimo m'miyoyo yathu? *Ndi chinthu chofunika kulola wina aliyense kukhala ndi mwayi kuti ayese Mawu a Mulungu pamenepa. Inu monga mtsogoleri musatsutse kapena kulola wina wake kutsutsa. Nkwabwino kulola aliyense kufotokozera za kukhosi.*

3. Yesu anabatizidwa, koma pakuti Iye ndiye Mulungu, sanachimwe.

Izi zitiuza kuti ubatizo sichipembedzo chinthu chimene chingakhoze kutichotsera machimo a munthu. Ngati cholinga cha ubatizo chinali kuyeretsa munthu ku machimo, Yesu sakanatha kubatizidwa, chifukwa Iye, monga Mulungu sanachimwepo.

4. Nthawi imene Yesu anatuluka m'madzi, Mzimu Woyera anatsika natera pa Iye monga nkhunda, ndi Mulungu Atate analankhula mawu kuchokera kumwamba akunena, "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera." Apa tikuona Utatu wake wa Mulungu. Kodi eni atatuwa ndi ayani?

   Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera.

5. Yesu anatengedwa kupita ku chipululu kukayesedwa ndi Satana. Satana alipo kweni-kweni. Iye ndi mzimu umene uli m'dziko pamodzi ndi otsatira ake, adielekezi, ndipo abweretsa chisokonezo m'miyoyo yathu potitsogolera ife kusamvera Mulungu. Monga momwe Yesu anayesedwa, Satana amatiyesa ife. Koma Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti ife, osafanana ndi Yesu, timayesedwenso ndi zoipa zokhazikika m'mitima yathu kuti tichite zinthu zosakondweretsa Mulungu.

6. Mneneri Yesaya analosera kuti Yesu adzakhala ngati kuwala kwa anthu amene anali mu mdima, kwa iwo amene anakhala mu mthunzi wa imfa.

Kopanda Yesu, ife tonse tili mu mdima, koma mwina inu kapena wina amene mumakonda amakhala mu mthunzi wa imfa. Ena amapezeka m'mthunzi wa imfa chifukwa cha mankhwala oipa osokoneza bongo, ena chifukwa cha khalidwe loipa, enanso chifukwa cha chiwawa, kapena zifukwa zina. Ndime imeneyi ikutiuza kuti Yesu anabwera kudzapereka kuwala kwa iwo amene ali mu mdima, ndipo Iye akhoza kupereka ufulu kwa iwo okhala mu mthunzi wa imfa.

*Mu pemphero lathu lero tipempherere okondedwa athu amene amakhala mu mthunzi wa imfa. Tonse tipeze kuwala ndi ufulu mwa Yesu Khristu.

Uthenga Wabwino wa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Zozizwitsa za Yesu – Phunziro 3, Mateyu 4-9

"Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu" Mateyu 4:19

KUBWEREZA

1. Ndani anafotokozera Yosefe za kubadwa kwa Yesu namuuza kuti dzina lake lidzakhala "Emanuele" kapena "Mulungu ali nafe?" Dzinali litiuza kuti Yesu ali nafe liti?
2. Ndani anafuna kupha mwana Yesu? Chifukwa chiyani? Yesu ndi makolo ake anapulumuka pothawira kuti?
3. Amene anambatiza Yesu anali yani? Pakuona kuti Yesu anabatizidwa, kodi cholinga cha ubatizo ndi kuyeretsa tchimo m'miyoyo yathu?
4. Pamene Yesu anatuluka m'madzi wina anatsika ngati nkhunda nkuthera pa Iye ndiponso mawu anamveka kochokera kumwamba. Nkhundayo inali ndani? Mawu anali a yani?
5. Afarisi anaganizira kuti sanayenere kulapa machimo chifukwa iwo anali opembedza. Kodi ndi kotheka kuti wina akhoza kukhala wachipembedzo chokwanira kuti machimo ake afafanizidwe?
6. Kodi liwu lakuti "kulapa" litanthauza chiyani?
7. Kodi tchimo ndi chiyani?
8. Ndani anamuyesa Yesu m'chipululu?
9. Kodi Yesu anapita kuti atabwerera ku chipululu?

Pamene Yesu anayenda m'mbali mwa nyanja ya Galileya anapeza asodzi awiri. Yesu anawaitana nanena, "Tsatani ine ndipo ndidzakusandutsani asodzi a anthu." Mofulumira anasiya makoka awo namtsatadi Iye. Tsiku lomwelo Yesu anaitana ophunzira ake anayi: Petro, Andrea, Yakobo ndi Yohane. Onsewo anali asodzi.

Tsono Yesu anapita m'dera lonse lozungulira Galileya kuphunzitsa m'nyumba zamapemphero kulalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu, ndi kuchiritsa nthenda za mitundumitundu pakati pawo. Anthu ambirimbiri anamtsatira Iye kulikonse kumene anapita.

Munthu wakhate anabwera kwa Yesu namgwadira Iye, nanena, "Ambuye, mukafuna mungandichiritse." Yesu anamuyankha, "Ndikufuna, chira!" Pomwepo anachiritsidwa.

Mkulu wa gulu la asirikali a Chiroma anabwera kwa Yesu. Munthu ameneyu anapempha Yesu kuti achiritse mnyamata wake amene analikudwaladi. Iye anakhulupirira mu mphamvu za Yesu za kumchiritsa. Yesu anamuuza iye kuti anthu ambiri amitundu yina yonse adzabwera kudzadya naye mu Ufumu wake wa Kumwamba. Mnyamatayo anachira mu ola lomwelo.

Nthawi yina ku tsidya la nyanja, m'dera la Agadara munali anthu awiri amene anagwidwa ndi ziwanda. Anthuwo anali aukali kwambiri, kotero kuti panalibe munthu wina aliyense amene anatha kuwagwira, ngakhale kuyenda pafupi pa iwo. Anakhala ku manda.

Atamuona Yesu, anthu awiriwo anapfuula, nati, "Tili nanu chiyani Inu, Mwana wa Mulungu? Kodi mwabwera kuno kudzatizunza ife nthawi isanakwane?"

Pamtunda pa iwo panali gulu lalikulu la nkhumba. Ziwandazo zinapempha Yesu kuti, "Mukatitulutsa, bwanji mutitume ife kuti tikalowe m'gulu la nkhumbalo." Yesu anziuza ziwandazo kuti, "Chabwino, pitani!" Nthawi yomweyo ziwanda zinatulutsidwa kwa anthuwo nalowa mwa nkhumba. Zitalowedwa ndi ziwanda, nkhumba zinakhala ndi misala. Zinathamangira kunsi kuphompho m'nyanjamo ndipo zinafa m'madzi.

Oweta nkhumbazo anathamanga nawauza onse okhala m'mudzi umenewo nafotokozera zonse zimeneYesu anachita, ndiponso zimene zinachitika ndi anthu ogwidwa ndi ziwanda. Anthu a mudziwo anatuluka kukakumana ndi Yesu napempha Iye kuti achoke kudera kwawo.

Yesu anachoka pa bwato nabwerera ku mzinda kwake. Pambuyo pake posachedwa, Iye anakomana ndi munthu wotchedwa Mateyu. Mateyu anali pa ntchito m'kanyumba pokhometsa misonkho ya boma. Yesu ananena kwa iye, "Unditsata ine." Nthawi yomweyo Mateyu anaimirira namutsatira Yesu.

Tsono Yesu ndi otsatira ake anapita masana kunyumba kwa Mateyu kukadya chakudya cha masana. Anthu ambiri okhometsa misonkho ndi anthu ena a mbiri zoipa anadya nawo. Pamene anthu a chipembedzo ndi Afarisi anaona zimenezi anawafunsa otsatira ake a Yesu, "Nchifukwa chiyani mphunzitsi wanu akudya ndi okhometsa misonkho ndi ena ochimwa?"

Pokumva zonena zawo, Yesu anawayankha Afarisi, “Iwo amene sadwala safuna sing’anga ayi, koma iwo odwala ndiwo ofuna sing’anga. Koma kamvetsetseni mawu a Mulungu aja akuti, ‘Ndimafuna chifundo, osati nsembe ayi.’ Pakuti sindinabwere kudzaitana anthu olungama, koma anthu ochimwa kuti alape natembenuka mtima.”

MAFUNSO

1. Kodi ophunzira oyamba a Yesu anali a ntchito yotani?
2. Kodi iwo anachita chiyani pamene Yesu anawaitana kuti amtsatire Iye?
3. Yesu anapita ku madera onse a ku Galileya ndi unyinji wa anthu unamtsatira Iye. Kodi Yesu anachita chiyani kuti anthu achite chidwi ndi kumtsatira Iye?
4. Kuchiritsa koyamba kolembedwa m’buku la Mateyu kumene Yesu anachita kunali chiyani?
5. Ndi vuto lotani limene mnyamata wa mkulu wa gulu la asirikali a Chiroma anali nalo?
6. Kodi anthu awiri amene anagwidwa ndi ziwanda anakhala kuti? Anali anthu otani?
7. Zitamuona Yesu, kodi ziwanda zija zinachita chiyani?
8. Chinachitika chiyani ndi ziwanda zitatulutsidwa ndi anthu awiriwo?
9. Chinachitika chiyani ndi nkhumba?
10. Kodi oweta nkhumbazo anachita chiyani?
11. Kodi Mateyu anagwira ntchito yotani?
12. Mu nkhaniyi ya Baibulo, kodi Yesu anadya pamodzi ndi anthu otani?
13. Kodi Afarisi anaganizira chiyani za izi?
14. Kodi Yesu anawayankha Afarisi bwanji?

ZOONA ZA UZIMU

1. <u>Yesu salekanitsa magulu a pakati pa anthu</u>.
   *Ophunzira oyamba a Yesu anali asodzi, anthu wamba amene sanaphunzire ku sukulu.
   *Wakhate anali munthu amene anachotsedwa pakati pa anthu ake chifukwa cha nthenda ya khungu imene inamuonetsera iye kusaoneka bwino ndipo ananyozedwa ndi anthu.
   *Mnyamata wake wa msirikali wa Chiroma anali munthu amene sanathe kuyenda. Anali munthu wamba ndipo analibe ndalama.
   *Mateyo anali wokhometsa misonkho. Anali wachuma, komabe mwina anali wakuba wokonda ziphuphu.
   *Anthu ogwidwa ndi ziwanda ananyozedwa kwambiri ndi anansi awo. Mwina anansiwo akadafuna kusunga nkhumba zawo koposa kuti ogwidwawo achiritsidwe. Onani, anayenera kukhala ku manda!

*Komatu anthu onsewa anali ofunikira kwa Yesu. Inu ndinu munthu wapadera ndi wofunika pamaso pa Mulungu. Katundu wanu, chuma chanu, zakale zanu, kapena maonekedwe anu ku malo amene mukupezeka: zonsezi nzosapindula pamaso pa Mulungu.

2. Yesu ali ndi mphamvu zochiritsa nthenda zathu. Kodi zitsanzo zina za anthu amene anachiritsidwa mu nkhaniyi ya Mawu a Mulungu ndi ziti?

3. <u>Yesu ali ndi mphamvu zopambana mzimu uliwonse kapena ziwanda</u>. Alipo anthu ena amene agwidwa ndi ziwanda kapena mizimu yoipa. Nthawi zina izi zimachitika pamene akuyesa kuchita zabwino. Koma iwo asanadziwe zimene zinachitika kwa iwo, ziwandazo zakopa kale m’miyoyo yawo. Amalondedwa na zunzidwa ndi ziwanda nthawi zonse. Anthuwa alibe mphamvu zochotsa ziwanda m’miyoyo yawo. Yesu ali ndi ulamuliro wopambana mzimu uliwonse kapena ziwanda. Tingakhale ndi ufulu ku mizimu yoipa kupyolera mwa Yesu yekha!

4. <u>Yesu amakonda anthu a mbiri zoipa. Amalandira onse ochimwa</u>. Yesu satsutsa anthu, koma chifuniro chake ndi kubweretsa munthu aliyense ku kulapa ndi kukhululu-kidwa kwenikweni.

5. Anthu a chipembedzo, monga Afarisi amene sanalape machimo awo, anaganizira kuti anali abwino koposera anthu ena ochimwa amene anadya ndi Yesu. Kodi chabwino ndi chiti: kukhala wochimwa wamkulu amene wakhululukidwa kapena kukhala munthu wokhala ndi machimo ochepa koma wokana kulapa?

*Ndi chabwino chapatali kukhala munthu wochimwa kwambiri amene machimo ake anakhululukidwa.

Yesu amatilandira ndi kutikonda ife monga momwe tilili. Kwa Iye, kulibe kanthu ngakhale ife takhala ochimwitsitsa, ngati tili aumphawi, ngati tili ndi maphunziro ochepa, ngati tili ndi mavuto ambiri kapena tili ndi nthenda. Pamaso pake, tonse tili ofanana. Chinthu chofunikira ndi kulapa ndi kutsatira Iye.

Uthenga Wabwino wa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Zophunzitso za Yesu – Phunziro 4, Mateyu 10-16

"Ndikufuna chifundo, si nsembe ayi." Mateyu 4:19

KUBWEREZA

1. Yesu anabadwira m'fuko la Chiyuda kwa mzimayi wotchedwa ndani?
2. Anthu anzeru a kum'mawa anatha kupeza Yesu chifukwa anatsogoledwa ndi chiyani?
3. Mulungu anawachenjeza bwanji anthu anzeru a kum'mawa kuti sayenera kubwerera ku Herode koma kuti anayenera kubwerera kwawo pa njira yina.
4. Yohane Mbatizi anakhala m'chipululu. Kodi anawachitira chiyani anthu amene anovomereza machimo awo?
5. Liwu lakuti "kulapa" likutanthauza chiyani?
6. Pamene Yesu anabatizidwa, wina anatsika ngati nkhunda nkutera pa Iye ndiponso mawu anamveka kochokera kumwamba. Kodi nkhundayo inali ndani? Kodi mawu ochokera kumwamba anali a yani? Izi zimationetsera Utatu wa Mulungu**.** Kodi anthu atatu mwa Mulungu ndi ayani?
7. Pamene anali m'chipululu, kodi Yesu anayesedwa ndi yani?
8. Ophunzira oyamba a Yesu anagwira ntchito yotani?
9. Yesu anakomana ndi anthu awiri ogwidwa ndi ziwanda. Kodi Yesu anawathandiza anthuwo bwanji? Kodi anthu a kumudzi kwawo anachita chiyani?
10. Afarisi anadandaula Yesu chifukwa anadya ndi anthu otani?
11. Kodi chabwino ndi chiti: kukhala wochimwa wamkulu amene analapa, kapena kukhala munthu wa machimo ochepa koma wosalapa?

Yesu anaitana anthu khumi ndi awiri kuti akhale ophunzira ake, Liwu lakuti "ophunzira" likutanthauza kuti anakhala pafupi ndi Yesu ndipo Iye anawaphunzitsa iwo. Iye anawapatsa mphamvu kupambana mizimu yoipa. Anawapatsanso mphamvu kuchiritsa matenda osiyana-siyana. Anawafotokozera iwo kuti ayenera kupereka mwaulere monga momwe iwonso analandira mwaulere. Yudasi Iskariote anali mmodzi wa anthu omwe amene anatumizidwa.

Yesu anawatumiza ophunzira ake kwina kulikonse m'dera la Israele ndi cholinga chofuna kuti anthu Aisraele alape ndi kukhulupirira Yesu Khristu. Yesu anawapatsa iwo uthenga kuti, "Yense amene adzavomereza Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzamvomereza iye pamaso pa Atate wanga wa Kumwamba. Koma yense amene adzandikana Ine, inenso ndidzamkana iye pamaso pa Atate."

Ndipo Yesu mwini wake anayenda m'Galileya monse kuphunzitsa, kulalikira, ndi kuchiritsa nthenda za mitundu yonse. Koma anthu a ku Galileya amene anali naye nthawi zambiri anakana uthenga wake. Mu mzinda wa Kapernao, kumene Yesu anayamba utumki wake, anthu anamukana Iye. Pakuona izi Yesu anapita kukalankhula ndi Atate wake nati,

> "Atate, Mwini Kumwamba ndi dziko lapansi, ndikuyamikani kuti munazibisira izo kwa anzeru ndi akudziwitsa, ndipo munaziululira zomwe kwa makanda; etu Atate chifukwa chotero chinakhala chokondweretsa pamaso panu. Zinthu zonse zinapere-kedwa kwa Ine ndi Atate wanga; ndipo palibe munthu adziwa Mwana, koma Atate yekha; ndi palibe wina adziwa Atate, koma Mwana yekha, ndi iye amene Mwana afuna kumuululira. Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzaku-pulumutsani inu. Senzani goli langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndili wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti goli langa lili lofewa, ndi katundu wanga ali wopepuka."

Atatha kunena izi zonse, Yesu ndi ophunzira ake anayenda napitirira minda ya tirigu. Ili linali tsiku la Sabata. Ophunzira ake anali ndi njala, ndipo anaima, natola tirigu wina nadya.

Afarisi (kumbukirani kuti iwowa anali anthu akulu a chipembedzo) pakuona zimenezi anawadzudzula Yesu ndi ophunzira ake pakuti chinali chinthu chosaleka kugwira ntchito pa tsiku la Sabata. Yesu anawayankha iwo nanena kuti iwo sathabe kumvetsa lamulo la Mulungu chifukwa malembo ananena, "Ndikufuna chifundo, si nsembe ayi."

Kuchokera ku munda wa tirigu Yesu ndi ophunzira ake anapita ku nyumba yopempherera-mo ya Ayuda ndipo komweko anampeza munthu wopuwala dzanja. Yesu anamuuza iye kuti atambasule dzanja lake ndipo anamchiritsa iye m'nyumba yopempherera-mo momwemo poyera pa tsiku la Sabata.

Afarisi anatuluka pa malopo moopsya mtima nakachita upo kuti apangane dongosolo lomuphera Iye. Yesu, pakudziwa maganizo awo anatulukanso pa malopo. Koma khamu lalikulu linamutsatira. Yesu anawachiritsa iwo onse nawalimbitsira mawu kuti asamuulule Iye.

Yesu anapitiriza kugwira ntchito kudera kumeneko kwa nthawi yochulukirapo kuphun-zitsa anthu nachiritsa nthenda zawo. Kokwanira kawiri, anthu anamtsatira Iye m'chipululu nakhala naye nthawi yayitali pakumva mawu ake ngakhale sanadye kanthu. Kokwanira kawiri, Yesu anatenga mikate yosachepera isanu ndi iwiri ndi tinsomba tochepa ndi kudyetsa anthu oposa zikwi zinayi.

Pogwirabe ntchito ku Galileya, Yesu anawafotokozera anthu omtsatira Iye kuti posachedwa Iye adzapita ku Yerusalemu, ndipo zinthu zina zoopsya zidzamuchitikira Iye kumeneko. Anawafotokozera kuti iwo adzavutitsidwa mu zinthu zambiri m'manja mwa atsogoleri a Chiyuda, ndi kuti Iye adzaphedwa, koma pamene masiku atatu atatha, Iye adzaukanso nadzakhala ndi moyo.

MAFUNSO

1. Kodi Yesu anapereka ntchito yotani kwa ophunzira ake?
2. Kodi Yesu ananena kuti adzawachitira chiyani iwo amene adzamuvomereza Iye pamaso pa anthu? Nanga adzawachitira chiyani iwo amene adzamkana Iye pamaso pa anthu?
3. Kodi anthu a ku Kapernao ndi mizinda yina kumene Yesu anachita zozizwitsa zambiri, anachita chiyani ndi uthenga wake wa Yesu?
4. Yesu ananena kuti iwo olema ndi othodwa abwere kwa Iye. Kodi Yesu amalonjeza kuti adzawachitira chiyani anthuwo?
5. Ndi chifukwa chiyani Yesu ndi ophunzira ake anaima pa munda wa tirigu?
6. Ndi chifukwa chiyani Afarisi anadzuzula Yesu pobudula tirigu?
7. Ndi chifukwa chiyani Afarisi ananyoza Yesu pamene anachiritsa munthu amene anali wopuwala dzanja?
8. Kodi cholinga chinali chiyani cha upo umene unakonzedwa ndi gulu la Ayuda?
9. Yesu anauza omtsatira Iye kuti zinthu zina zidzamchitikira Iye. Ulosi wake unali chiyani?

ZOONA ZA UZIMU

1. Aliyense amene adzavomereza Yesu pamaso pa anthu, Yesu adzamvomereza iye pamaso pa Atate. Koma iye amene adzakana Yesu pamaso pa anthu, Yesu adzamukananso iye pamaso pa Atate wa Kumwamba.

2. Anthu ambiri anamtsata Yesu chifukwa chabe anafuna chozizwitsa china chochokera kwa Iye, koma sanafune chibale naye, ndipo sanafune kumvera mawu ake. Sanafune kulapa machimo awo. Anangofuna kupeza mwayi woti Mulungu awachitire chifundo. Kodi anthu otero alipobe masiku ano? Kodi mumadziwa chifukwa chiyani?

3. Munthu yekhayo wotha kufika kwa Atate ndi Yesu Khristu ndi iwo amene amafikira kwa Atate kupyolera kwa Yesu. Kulibenso wina amene amatipempherera ife kwa Mulungu koma Yesu yekha. Alipo Mulungu mmodzi yekhayo, ndipo njira ndi imodzi yofikira kwa Iye. Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti njira imeneyo ndi Yesu yekha.

*Mwina mwaphunzitsidwa kupemphera kwa Mulungu kupyolera mwa anthu ena okupempherera koposera Yesu. Kodi enawo otipempherera ife ndi ayani? Ndiwo milungu yina? Aneneri? Anthu oyera mtima akale? Mawu a Mulungu anena kuti pamakhala anthu ena abwino, koma iwo si Mulungu. Kodi mukugwirizana ndi zimene Mawu a Mulungu anena kuti pali njira imodzi yotipempherera pakati pa Mulungu ndi munthu: Yesu Khristu?

4. Yesu amafuna kunyamula mitolo ndi madandaulo athu. Iye ndi wofatsa ndi wodzi-chepetsa mtima. Amafuna kuti atipeputse ife ku mitolo yathu. Mwa iye tingapeze mpumulo wa miyoyo yathu ngati ifeyo tivomereza goli lake. Tiyenera kuvomereza umbuye kapena utsogoleri wake m'miyoyo yathu.

5. Yesu ali ndi nkhawa ya zosowa zathu za thupi. Ophunzira ake a Yesu anamva njala ndipo Yesu anawapatsa iwo chakudya, ngakhale anadziwa kuti ichi chidzakhwiyitsa Afarisi. Mulungu, Mlengi wa zonse ali ndi nkhawa ya zosowa zathu za thupi za ife tonse.

"Ndikufuna chifundo, si nsembe ayi." Liwu lakuti "nsembe" litanthauza chiyani kwa inu? Kodi mwaphunzitsidwapo ndi akulu a chipembedzo kuti mupereke nsembe kwa Mulungu kuti mukhululukidwe tchimo lina kapena kulandira chifundo china? Kodi ndi chinthu chovuta kwa inu kukhulupirira kuti Mulungu sakufuna kuti mutsimikizire chilichonse kwa Iye pakupereka nsembe? Iyi ndi nthawi yachiwiri imene Yesu akuyesa kufotokozera Afarisi kuti Mulungu sakondwera ndi nsembe za munthu. Koma anthu amene amakhala oonetsa ngati opembedza amavutika kumvetsa ndi kuvomereza. Zipembedzo zonse zimaphunzitsa kuti tiyenera kuchita chinthu china chake kuti tipewe mkhwiyo wa Mulungu kapena kulandira chifundo chake. Anthu ambiri amayenda m'mavuto kuyesa kuti alipirire Mulungu kubwereza malonjezano ake amene anachita, kapena kulipirira machimo awo a mbuyo, komanso mwina kuonetsera umvano wawo. Koma zinthu zonsezi sizingathe kukondweretsa Mulungu. Iye akufuna chibale ndi ife. Akufuna kutionetsera chifundo; Safuna nsembe zathu. Yesu anazindikira kuti adzamva zowawa zambiri ndiponso kuti pal mbuyo adzafa. Koma patatha masiku atatu Iye adzauka kwa akufa. Zonsezi zinali mu dongosolo la Mulungu. Anayesera kufotokozera izi kwa ophunzira ake, koma iwo sanamvetse chifukwa choti Yesu anayenera kufa naukanso.

*M'maphunziro atatu otsiriza amene tidzaphunzira, tidzayesa kuzindikira kufunikira kwa imfa ya Yesu ndi kuuka kwake kwa akufa. Chochitika chapaderachi chinasintha mbiri yonse ya dziko mpaka muyaya ndipo chili ndi mphamvu yophwanya ukapolo wa tchimo ndi kusintha miyoyo yathu.

Uthenga Wabwino wa Yesu

Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu

Kuperekedwa Kwake Kwa Yesu – Phunziro 5, Mateyu 20-26

"Ndipo pamene Yesu analikukwera ku Yerusalemu, anatenga ophunzira khumi ndi awiri napita nawo pa okha, ndipo panjira anati kwa iwo, 'Onani, tikwera ku Yerusalemu ; ndipo Mwana wa munthu adzaperekedwa kwa ansembe akulu ndi alembi, ndipo iwo adzamweruza kuti ayenera imfa, nadzampereka kwa anthu akunja kuti amnyoze ndi kumkwapula, ndi kumpachika; ndipo Iye adzaukitsidwa tsiku lachitatu." Mateyu 20:17-20

KUBWEREZA

1. Kodi Yesu anabadwa ndi namwali wotchedwa ndani?
2. Bambo wake, Yosefe, analota loto limene Mulungu anamuuza kuti athawire ku Ejipito chifukwa mfumu Herode anafuna kuchita chiyani ndi Yesu?
3. Yohane Mbatizi anakhala m'chipululu. Analalikira nawabatiza iwo amene anachita chiyani ndi machimo awo?
4. Yesu anapempha Yohane kuti ambatize Iye. Kodi Yesu anali ndi tchimo?
5. Kodi liwu lakuti "kulapa" litanthauza chiyani?
6. Pamene Yesu anabatizidwa ndani anatsika pa Iye monga nkhunda? Pomwepo anthu anamva mawu a Mulungu ochokera kumwamba. Kodi Mulungu ananena kuti amakondwera ndi yani?
7. Kodi Yesu anayesedwa ndi yani pamene anali m'chipululu?
8. Yesu anakomana ndi anthu awiri amene anagwidwa ndi ziwanda. Kodi Yesu ali ndi mphamva zopambana ziwanda?
9. Kodi chabwino ndi chiti: kukhala wochimwa wamkulu amene analapa, kapena kukhala munthu wa machimo ochepa koma wosalapa?
10. Kodi Yesu ananena kuti adzawachitira chiyani iwo amene adzamuvomereza iye pamaso pa anthu?
11. Anthu a ku Galileya anatsata Yesu chifukwa chabe cha zozizwitsa zimene anachita. Kodi mukuganiza kuti anagwirizana ndi Mawu a Mulungu?
12. Anthu a ku Galileya sanafune kulapa machimo awo. Tiyeni tibwerezenso: Kodi liwu lakuti "kulapa" litanthauza chiyani?
13. Yesu ananena kuti adzapatsa chiyani kwa iwo amene akulema ndi akuthodwa? Ananena kuti goli lake ndi lotani?
14. Ndi chifukwa chiyani Afarisi sanafune Yesu kuchiritsa munthu wopuwala dzanja?
15. Afarisi aja anapangana dongosolo lochita chiyani ndi Yesu?
16. Ngakhale Yesu anadziwa kuti Afarisi anafuna kumupha, anapitiriza kuchita zozizwitsa zina. Kodi Yesu anadyetsa anthu okwanira zikwi zinayi ndi chiyani?

Yesu ndi ophunzira ake anayenda kuchokera ku Galileya kupita ku Yerusalemu. Pamene anali pafupi ku Yerusalemu Yesu anapempha awiri a ophunzira ake kupita ku mudzi wina kukapeza bulu amene Iye anafuna. Yesu anakwera pamwamba pa bulu ulendo wolowa mu Yerusalemu.

Yesu analowa m'Yerusalemu mwa ulemerero. Khamu la anthu linamzungulira Iye m'mbali zonse za msewu. Anthu ambiri anayala zovala zawo pa njira kupanga chopondera kuti Yesu alowe mu mzinda. Ena anadula nthambi za kanjedza naziyala m'njiramo kupereka ulemu. Ndipo anthu ochuluka amene anali patsogolo ndi amene anali m'mbuyo anafuula kuti, "Hosana Mwana wa Davide! Wolemekezeka Iye akudza m'dzina la Ambuye! Hosana m'Kumwambamwamba!"

Mzinda wonse wa Yerusalemu unatekeseka ndi zimene zinachitika. Aliyense anafunsa m'mzindamo, "Kodi uyu ndi yani? Anthu ambiri anayankha, "Uyu ndi Yesu, mneneri wochokera ku Nazarete a ku Galileya."

Tsono Yesu analowa m'mzinda napita ku kachisi wa Ayuda. Kumaloko Yesu anatulutsira anthu a malonda; anagubuduza matebulo a iwo osintha ndalama amene anapanga kanyumba kawo m'kachisimo. Anawauza kuti, "Zalembedwa, 'Nyumba yanga idzatchedwa nyumba yopemphereramo koma mwaisandutsa phanga la achifwamba.'" Pambuyo pake pa izi anatsala m'kachisi nachiritsa iwo akhungu ndi opunduka.

Yesu anawaphunzitsa anthu ambiri zinthu zambiri nachita zizindikiro ndi zozizwitsa zina. Ansembe akulu ndi atsogoleri a chipembedzo anasonkhana nakhala upo wakuti amgwire Yesu ndi chinyengo namuphe. Koma sanafune kumupha Iye nthawi ya chikondwerero cha Paska chifukwa anadera nkhawa pangazachitike chipolowe pakati pa anthu. Tsono anagwirizana kuti amupha Yesu itadutsa nthawi ya Paska.

Wina wa ophunzira ake, wotchedwa Yudasi Iskariote anakomana ndi ansembe akulu nafunsa, "Mundipatsa chiyani ndikampereka Yesu m'manja mwanu?" Anagwirizana nampatsa Yudasi ndalama za siliva makumi atatu. Ndipo kuyambira pamenepo anafuna kupeza mwayi woti atha kumperekera Yesu m'manja mwawo

Itangokwana nthawi ya Paska, ophunzira anakonza phwando monga momwe Yesu anawalangizira. Pa tsiku la chikondwerero Yesu anakhala pansi pamodzi ndi khumi ndi awiri aja nanena kwa iwo, "Zoonadi ndinena kwa inu, mmodzi wa inu adzandipereka ine." Atangotha kunena izi ophunzira aja anagwidwa ndi chisoni ndipo aliyense anayamba kufunsa, "Ambuye, kodi ndi ine?"

Yesu anayankha nanena, "Iye amene atsutsa nthongo limodzi ndi ine yemweyo adzandipereka ine. Mwana wa munthu adzapita monga momwe kunalembedwa kwa Iye, koma tsoka kwa iye amene adzapereka Mwana wa munthu! Kukadakhala bwino kwa munthuyo ngati sakadabadwa."

Yudasi, yemwe mmodzi anampereka Iye, anamfunsa Yesu, "Mphunzitsi, kodi ndi ine?" Yesu anamuyankha kuti, "Wanena wekha."

Choncho anadya limodzi mgonero masana. Nthawi imene analikudya, Yesu anatenga mkate naudalitsa naunyema nanena, "Tengani, idyani. Ili ndi thupi langa." Chomwecho anatenga chikho, nayamika ndi kupatsa kwa iwo nanena, "Imwani awa, inu nonse. Popeza awa ndi magazi a chipangano chatsopano chimene chifafaniza machimo ochuluka."

Atatha kudya chakudya, anayimba nyimbo ndiponso onse anapita limodzi ku phiri la Azitona. Komweko Yesu anapitiriza kuwaphunzitsa zina zidzachitika posachedwa.

Tsopano Yesu anapita ndi ophunzira ake aja ku malo otchedwa Getsemani kuti apemphere limodzi usiku wonse. Ndipo anatenga Petro, Yakobo ndi Yohane pamodzi naye , ndipo anayamba kugwidwa ndi chisoni. Anawapempha iwo kuti akhale nachezere naye. Posachedwa anamuka patsogolo pang'ono kuti apemphere pa yekha ndi Atate wake. Anapemphera usiku zokhudza zimene zikubwera pa Iye. Mawu ake analembedwa motere:

> "Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire ine; koma si monga ndikufuna ine, koma Inu."

Kunalembedwa kuti Iye anapemphera pemphero lomwelo katatu, mtima wake unali ndi chisoni chapafupi imfa.

Komabe ophunziriwa sanathe kutsegula ngakhale maso awo ata pang'ono. Onse anagona tulo. Potsiriza Yesu anauka nawauza kuti, "Dzukani. Tiyeni tizipita. Onani, wondipereka ali pafupi."

MAFUNSO

1. Pamene Yesu analowa m'Yerusalemu, kodi anakwera pa nyama yotani?
2. Anthu anamchitira Yesu chiyani nthawi imene analowa m'Yerusalemu?
3. Yudasi anachita chiyani kuti apereke Yesu?
4. Kodi ndi phwando liti limene anthu anachita m'mzinda nthawi yomweyo?
5. Kodi Yesu anachenjeza Yudasi bwanji kuti anadziwa kuti adzampereka Iye?
6. Kodi Yesu ananena chiyani za vinyo kuti anali chiyani nthawi ya mgonero?
7. Molingana ndi Yesu, kodi kofunika kwa kukhetsa mwazi kunali chiyani?
8. Yesu anawatenga ophunzira ake napita nawo ku Getsemani kukapemphera usiku wonse. Kodi analipo ophunzira angati amene anatha kuchezera naye usiku wonse?
9. Usiku umene Yesu anaperekedwa, kodi Yesu anapemphera chiyani?

ZOONA ZA UZIMU

1. Mulungu ndi woyendetsa zinthu zonse. Afarisi anapangana dongosolo lomgwirira Yesu. Koma Mulungu anawagwiritsa ntchito iwowo kuti achite chifuniro chake. Chinali cholinga chake cha Mulungu kuti Yesu adzafera pa mtanda.
2. Mulungu amadziwa zonse zimene zili m'mitima yathu. Palibe wina aliyense sadziwa. Yesu anadziwa nthawi yonse kuti Yudasi, wophunzira wake, adzampereka Iye.
3. Yesu amatikonda ndipo amationetsera chikondi chomwecho ngakhale ife timukana Iye. Yudasi anakhala bwino limodzi ndi Yesu ngakhale panalibe mmodzi wina mwa ophunzira ake amene anazindikira kuti adzakhala wompereka Yesu. Mu njira yomweyo, Yesu amatikonda nachita nafe mwa chikondi ngakhale nthawi zina timampereka Iye ndi kumkana Iye ndi chifuniro chake ku miyoyo yathu.
4. Mwazi wa Yesu unakhetsedwa chifukwa cha ife kuti machimo athu akhululukidwa ndi kuchotsedwa. Nthawi yomweyo, ophunzira ake a Yesu sanazindikire cholinga chakuti Yesu anayenera kufa. Sanazindikire kuti Mulungu amalamula munthu aliyense kulipira mphoto ya machimo ake ndiponso kuti mphotoyo ndi kukhetsa mwazi. Anazindikira kuti Yesu anawakonda ndipo machimo awo anakhululukidwa. Komabe inali patsogolo pamene iwo asanazindikire dipo limene Yesu anayenera kulipira kuti athe kukhululukira machimo.

*Anthu ambiri amazindikira kuti ali ndi tchimo m'mitima mwawo. Anthu ena amamvapo za mbiri ya Yesu, kuti anawakonda iwo. Koma ndi anthu ochepa amene amazindikira kuti Mulungu anaumirira munthu aliyense kulipira mphoto ya machimo ake ndiponso kuti mphotoyo ndi kukhetsa mwazi. Pakuti Yesu ndi Mulungu, Iye ndiye munthu mmodzi yekha wokhala pa dziko lapansi lino amene alibe tchimo ngakhale limodzi. Chifukwa cha chikondi chake chopambana kwa ife, Yesu anasankha kupereka moyo wake kukhala nsembe yolipira mphoto ya machimo. Si machimo athu okha ayi, koma machimo a anthu onse pa dziko lapansi. Ndi chifukwa cha nsembe imeneyi kuti tsopano tingakhululukidwe ku machimo athu ndi kukhala m'mtendere ndi Mulungu.

M'phunziro likubwera tidzaona mwa ndondomeko za kupachikidwa kwa Yesu.

Uthenga Wabwino wa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kupachikidwa Kwake Kwa Yesu – Phunziro 6, Mateyu 26-27

“Yesu anati kwa iye, ‘Mwatero, koma ndinenanso kwa inu, kuyambira tsopano mudzaona Mwana wa munthu ali kukhala ku dzanja la manja la mphamvu, ndi kufika pa mitambo ya kumwamba.’” Mateyu 26:64

KUBWEREZA

1. Kodi Yesu anabadwa ndi namwali wotchedwa ndani?
2. Monga momwe Malembo anenera, Yesu anabadwira ku mzinda kuti?
3. Monga momwe Malembo anenera, pothawa mfumu Herode, Yesu ndi banja lake anabwera kutuluka kupita ku malo otchedwa chiyani?
4. Bambo wake wa Yesu, Yosefe, analota loto limene anauzidwa kuti abwerere ku dziko la Israele pakuti mfumu Herode anafa. Koma chifukwa anaopabe mwana wake wa Herode, anasamutsa banja lake nakhala nalo ku mzinda wa Nazarete m’dera liti?
5. Yesu anayamba utumiki wake pobatizidwa ndi yani?
6. Pamene Yesu anabatizidwa, potuluka Iye m’madzi wina ngati nkhunda anatsika nkutera pa Iye. Yomweyo anali ndani? Ndiponso mawu anamveka kuchokera kumwamba nanena, ”Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa, mwa Iye ndakondwera.” Kodi mawu amenewo anali a yani?
7. Yesu anachiritsa anthu ambiri nawakhululukira iwo chiyani?
8. Ngakhale kunachitika zozizwa zambiri, anthu ambiri a ku Galileya sanafune kulapa machimo awo. Kodi anachita chiyani ndi uthenga wake wa Yesu?
9. Kodi liwu lakuti “kulapa” likutanthauza chiyani?
10. Nthawi imene Yesu analowa m’Yerusalemu kunali anthu ambiri oyenda naye. Kodi mwa ulendo umenewo Yesu anakwera pa chiyani?
11. Pokudya mgonero pa usiku wa chikondwero cha Paska, Yesu anawauza ophunzira ake kuti wina wa iwo adzachita chiyani ndi Iye?
12. Yesu analankhula za vinyo amene anamwa. Ananena kuti vinyo anali kuimirira mwazi umene udzakhetsedwe chiyani?
13. Ngakhale anamva mawu ake a Yesu, ophunzira sanazindikirabe chimene Yesu adzachita ndi machimo awo. Chimenechi ndi chiyani?
14. Pambuyo pa mgonero, onse anapita ku phiri la Azitona kenaka ku Getsemane. Pamene Yesu anapemphera, kodi ophunzira ake anachita chiyani?
15. Yesu anapemphera kuti, “Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire Ine; koma si monga ndikufuna Ine, koma Inu.” Kodi Yesu anafuna chifuniro cha yani chichitike?

Pamene Yesu anadzutsa ophunzira ake, Yudasi, amene anampereka Iye, anafika ndi gulu lalikululu la anthu kuphatikizapo akulu a ansembe ndi atsogoleri a chipembedzo. Ambiri a iwo ananyamula malupanga ndi zibonga. Yudasi anabwera nampsyopsyona Yesu nampereka Iye moni. Yesu anamuyankha iye, “Mnzanga, wafikiranji iwe?”

Posachedwa mmodzi wa ophunzira ake anafika mofulumira nasolola lupanga lake nadula khutu la mmodzi wa atumiki ake a wansembe. Yesu anatontholetsa wophunzira uja natenga khutu namchiritsa mtumikiyo. Yesu anawauza ophunzira ake kuti akadafuna akanatha kuitanitsa gulu la angelo kubwera kudzamenyana nkhondo , koma zonse zimene zinachitika zinali chifuniro chake cha Mulungu kuti Malembo akwaniritsidwe.

Yesu anatembenukira ku gulu la anthu limene linabwera nawafunsa iwo, “Koma bwanji mwabwera kwa ine monga ngati wakuba ndi malupanga ndi zibonga? Ndinakhala nanu tsiku ndi tsiku kuphunzitsa m’kachisi koma simunandigwire ine. Koma izi zonse zachitika kuti Malembo a aneneri akwaniritsidwe.

Pomwepo ophunzira ake a Yesu anathawa mofulumira namusiya Iye pa yekha.

Tsono iwo amene anagwira Yesu anamtenga Iye napita naye ku nyumba ya munthu wotchedwa Kayafa amene anali mkulu wa ansembe. Pa nyumba yakeyo ansembe onse ndi atsogoleri a chipembedzo anadikirira Yesu kuti amfunse mafunso ambiri.

Anakonzekera kale maumboni ambiri a bodza kunenera Iye kuti aphedwe. Ndipo zoonadi, ambiri anabwera patsogolo, ngakhalabe analephera kupeza umboni weniweni

wokwanira kumupha mpaka mkulu wa ansembe anabwera namfunsa Yesu, “Ndikulumbiritsa iwe pa Mulungu wa Moyo kuti utiuze ife ngati iwe ndiwe Khristu, Mwana wa Mulungu!”

Yesu anati kwa iye, “Mwatero, koma ndinenenso kwa inu, kuyambira tsopano mudzaona Mwana wa munthu akukhala ku dzanja la manja la mphamvu ndi kufika pa mitambo ya kumwamba.”

Pomwepo mkulu wa ansembe anang’amba zovala zake nati, “Kunyoza Mulungu koopsatu!” Iwo anthu a m’gulu analavula pa nkhope pake nambwanyula Iye; ndipo ena anammenya Iye nampanda kofu nati, “Utilote ife, Khristu iwe, wakumenya iwe ndani?”

M’mawa wa tsiku linalo ansembe ndi atsogoleri a chipembedzo anamtenga Yesu kupita naye kwa mkulu wa Chiroma dzina lake Pilato. Anamfotokozera Pilato kuti Yesu anadzitchula Iyeyo ali mfumu ya Ayuda.

Pilato anamtenga ndi kumfunsa mafunso Iye, “Kodi iwe ndiwe mfumu ya Ayuda?” Yesu anayankha, “Pakuti inu mwatero.”

Ngakhale anamfunsa mafunso ambiri, Pilato sanathe kupeza chifukwa cha kumpachika Yesu. Komanso mkazi wake wa Pilato anazunzika ndi loto usiku wina za zonsezi namchenjeza mwamuna wake kuti asachite kanthu ndi Yesu. Pilato anazindikira kuti atsogoleri a Chiyuda anampereka Yesu m’manja mwake kungochita nsanje. Koma sanadziwe kuti achite chiyani chifukwa anthu anasokonozeka.

Chaka chilichonse mu nthawi ya Paska inali njira yake ya chizolowezi cha Pilato kuti atulutse mmodzi wandende amene anthu angasankhe. M’chaka chimenecho munali wandende woipititsa dzina lake Barabasi. Tsono Pilato anabweretsa Barabasi ndi Yesu napereka mpata khamu nati, “Modi mukufuna tikumasulereni yani, Barabasi kapena Yesu wotchedwa Khristu?” Koma anthu ovundulika ndi Afarisi anakuwa limodzi, “Barabasi!”

Pilato anafunsa, “Nanga ndidzachita chiyani ndi Yesu wotchedwa Khristu?” Anthu analira kwakulu, “Apachikidwe pa mtanda!”

Tsono Pilato, ataona kuti anthu anayamba chipolowe anatenga madzi nasamba manja ake nati, “Ine ndilibe kuchimwira mwazi wa munthu wolungama, mudzionere nokha.” Pomwepo anawamasulira iwo Barabasi, koma anakwapula Yesu nampereka Iye kwa iwo kuti ampachike pa mtanda.

Asirikali ake a Pilato anamtenga Yesu napita naye ku nyumba ya bwanamkubwa kumene anamzunza namlalatira Iye. Khamu lonse anamzungulira Yesu ndipo anavula malaya ake namveka Iye ndi malaya ofira achifumu. Ndipo analuka chisoti cha minga nachiika pa mutu pake, namgwiritsa ndodo m’dzanja lamanja lake; ndipo anagwada pansi pamaso pake nasewera naye mwa chipongwe nati, “Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda!” Anamthira malovu natenga ndodo nampanda Iye pa mutu. Atatha kusewera naye anavula malaya aja namveka Iye malaya ake napita naye ku malo otchedwa Gologota kapena “Malo a Chibade cha Mutu” kuti akampachike pa mtanda.

Yesu anapachikidwa kumeneko. Pamwamba pa mutu wake, Aroma analemba mawu akuti, “Uyu ndi Yesu, Mfumu ya Ayuda.” Anapachikidwa pakati pa mbala ziwiri mbali zonse za dzanja lake.

Nthawi inangokwana ola lachisanu ndi chimodzi kukafika pa ola lachisanu ndi chinayi pamene Yesu anali chipachikiridwe pa mtanda, mdima waukulu unakuta pa dera lonse padziko. Itangokwana ola lachisanu ndi chinayi Yesu analira nafuula, “Eli, Eli, lama sabakatani?” Kutanthauza kuti “Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji ine?” Patangotha nthawi yochepa Yesu analiranso nafuula ndi mawu akulu napereka mzimu wake.

Nthawi imene atangopereka mzimu wake, zinthu zambiri zozizwitsa zinachitika. Chinsalu cha m’kachisi chinang’ambika pakati kuchokera kumwamba kufikira pansi. Dziko linagwedezeka ndi miyala yambiri inang’ambika. Manda ambiri anatseguka, ndipo anatuluka anthu ambiri a Mulungu amene anamwalira kale, anauka kwa akufa. Anatuluka m’manda, ndipo Yesu, atauka kwa akufa, iwo analowa m’Yerusalemu naonekera ndi anthu ambiri.

MAFUNSO

1. Kodi Yesu anaperekedwa ndi Yudasi bwanji?
2. Wina wa iwo amene anali limodzi ndi Yesu anachita chiyani momteteza Iye? Pambuyo pake pa ichi, kodi Yesu anachita chiyani?
3. Pamene Yesu anaperekedwa m'manja mwa adani ake, kodi ophunzira ake anachita chiyani?
4. Kodi anthu a ku Getsemani anatengera Yesu kuti?
5. Ngakhale zinalipo mboni zonama zambiri, kodi anakhuza bwanji kunyoza Mulungu koopsatu kumene Yesu anamunenera?
6. Kodi atsogoleri a Chiyuda anamtengera Yesu kwa yani nthawi ya m'mawa?
7. Pilato atatha kumfunsa Iye mafunso, sanampezere Yesu chifukwa, koma anachita mantha ndi anthu. Tsono anapereka mpata kwa anthu. Kodi Pilato anawapatsa mpata wotani? Nanga anthu anasankha chiyani?
8. Kodi asirikali anachita chiyani ndi Yesu?
9. Pambuyo pa maola atatu kunali mdima, Yesu anafuulira kwa Mulungu. Mawu amene anafuula anali chiyani? Kodi kutanthauza kwake ndi chiyani?
10. Zinthu zina zimene zinachitika Yesu atapereka mzimu wake zinali ziti?

ZOONA ZA UZIMU

1. Yesu ndi yani? "<u>Mwana wa munthu akukhala ku dzanja la manja la mphamvu ndi kufika pa mitambo ya kumwamba</u>." Ili linali yankho limene Yesu anapereka kwa mkulu wa ansembe, ndipo linali yankho lakeli limene linamfikitsa Iye pa kumpachika. Linali yankho limene anthuwo sanathe kuvomereza. Koma aliyense ayenera kuvutika nalo yankho limeneli. Kodi Yesu ndi yani? Chifukwa ngati Yesu akukhala ndithu pa dzanja la manja la mphamvu, ndipo akubwera kumitambo kumwamba, ife tonse tiyenera kuganizira kuti chimene tidzamuyankha Iye ndi chiyani?
2. Yesu anapachikidwa m'malo mwake mwa Barabasi, mbala wozondedwa, ndipo Barabasi anamasulidwa nakhala mfulu.

*Mwina ine sindine mbala wozondedwa ngati Barabasi. Komabe, monga iye, ndine wochimwa. Pamaso pa Mulungu mphoto yanga ndi ya imfa. Mawu a Mulungu akufotokozera pa Aroma 6:23 kuti, "Mphoto yake ya uchimo ndi imfa." Izi zitanthauza kuti tonse tiyenera kulandira chilango cha imfa chifukwa cha zolakwa zimene tachita m'miyoyo yathu. Izi zilibe kanthu kaya tili ndi machimo ochuluka monga ngati Barabasi, kapena tikadakhala ndi moyo wabwino monga ena a ophunzira ake analili.

3. Yesu anatonzedwa, kuweruzidwa ndi kuphedwa kuti alipire chilango cha machimo m'miyoyo yathu. Ichi ndi chifukwa chakuti Yesu anabwera padziko, Iye anafuna kuti ife tidzathe kuima pamaso pa Mulungu kutikhululukira machimo athu onse. Anthu ambiri anamva kuti Yesu anali woyenera kuphedwa kapena kuti anali mneneri. Koma izi sizoona monga momwe Yesu anaululira. Anadzitchula yekha Mulungu ndi kuti anadza pa dziko lino kuti atifere ife machimo athu.

4. Yesu anapereka mzimu wake. Nthawi yina iliyonse Yesu akadathawa pa mtanda. Iye akadatha kupha anthu onse amene anamunenera zosayenera ngakhale liwu limodzi. Koma kupyolera ndi kusankha kwake, Iye anapirira modzichepetsa nakahala pa mtanda kufikira nthawi yake yokonzedweratu. Chomwecho mu nthawi yake anapereka mzimu wake. Iye anafuna kupereka ngongole ya machimo athu. Mawu a Mulungu akufotokoza pa Yohane 3:16 kuti, "Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha."

*Mu phunziro lina, tidzaphunzira za kuuka kwa Yesu. Choonadi ndi ichi kuti Yesu sali kufa koma kuti ali moyo, ndipo lero akufuna kulowa m'moyo mwanu. Akufuna kuyeretsa mtima wanu ku machimo ndi kukusinthani inu kwatunthu.

Uthenga Wabwino wa Yesu
Nkhani Zoona Zochokera mu Buku la Mateyu
Kuuka Kwake Kwa Yesu – Phunziro 7, Mateyu 27-28

“Musaope inu; pakuti ndikudziwa inu mulikufuna Yesu, amene anapachikidwa. Iye mulibe muno iyai; pakuti anauka, monga ananena…” Mateyu 28:5,6

KUBWEREZA

1. Yesu anabadwa ndi namwali wotchedwa ndani?
2. Yesu anayamba utumiki wake wa poyera pamene Yohane Mbatizi anamuchitira Iye chiyani?
3. Pamene Yesu anabatizidwa, wina anatsika ngati nkhunda nkutera pa Iye ndiponso mawu anamveka kochokera kumwamba. Nkhundayo inali ndani? Mawu ochokera kumwamba anamutcha Yesu ndani? Izi zimationetsera Utatu wa Mulungu**.** Kodi anthu atatu mwa Mulungu ndi ayani?
4. Yesu anachiritsa anthu ambiri odwala nthenda ndi kukhululukira chiyani anthu ambiri?
5. Ngakhale Yesu anachita zozizwitsa zambiri, anthu ambiri okhala m’dera la Galileya sanalandire mawu ake nakana kuchita chiyani ndi machimo awo?
6. Liwu lakuti, “kulapa” likutanthauza chiyani?
7. Yesu ananena kuti vinyo wa mgonero aimira chiyani? Mgonero umenewo udzachita chiyani?
8. Afarisi anagwira Yesu ku Getsemani pamene analikupemphera namtenga Iye ku nyumba ya Kayafa, amene anali yani?
9. Mkulu wa ansembe anamfunsa Yesu kuti Iye anali yani? Yesu atayankha kuti anali ameneyo, anthu ena anamchitira Iye chiyani?
10. Nthawi ya ku m’mawa, Afarisi anatenga Yesu kwa bwanamkubwa wotchedwa ndani?
11. Pilato sanathe kupeza cholakwa mwa Yesu, koma analola kuti Yesu apachikidwe chifukwa chiyani?
12. Asirikali a Chiroma anamzunza Yesu. Anaika chiyani pa mutu wake? Anamumenya Iye ndi chiyani?
13. Pamene Yesu anapachikidwa pa mtanda, Aroma analemba pamwamba pa mutu wake mawu akuti chiyani?
14. Kuyambira pa ola khumi ndi chiwiri masana mpaka ola lachitatu, ndi chiyani chimene chinasowa?

Panali munthu wa chuma wa ku Arimatea dzina lake Yosefe amene analinso wophunzira wa Yesu. Yosefe anapempha Pilato kuti atenge mtembo wa Yesu nakaike m’manda mwake mwa iye mwini. Pilato anavomera ndipo Yesu anaikidwa m’manda mwatsopano. Yesu ataikidwa, chimwala chachikulu chinakunkhunizidwa ku khomo la manda.

M’mawa mwake Afarisi anakomana pamodzi napita pamaso pa Pilato chifukwa anakumbukira mawu amene Yesu ananena kuti Iye adzauka tsiku lachitatu. Anapempha Pilato kuti achinjirize manda kuti mwina mwake chinthu china chidzachitika ndi thupi lake la Yesu. Pilato anawalola kuti ayenera kulondera momwe angathere. Afarisi aja anapita ku manda nakhazika alonda pomwepo.

Pa tsiku loyamba la sabata Maria Magadala ndi Maria wina anapita ku manda kumene Yesu anagona. Mwadzidzidzi chinachitika chivomezi chachikulu, ndipo chimwala chija chinaguduzika. Mngelo wa Ambuye anakhala pamwamba pake. Alonda aja anachita mantha nayamba kunjenjemera nakhala ngati anthu akufa.

Koma mngelo analankhula mofatsa ndi azimayi awiriwo nanena, “Musaope inu; pakuti ndikudziwa kuti mukufuna Yesu, amene anapachikidwa. Iye mulibe muno iyayi; pakuti anauka, monga ananena. Idzani muno mudzaone malo m’mene anagonamo Ambuye. Ndipo pitani msanga, muuze ophunzira ake kuti wauka kwa akufa; ndipo onani, akutsogolerani ku Galileya; mudzamuona Iye komweko; onani, ndakuuzani inu.”

Azimayiwo anachoka msanga kumanda ndi mantha ndi kukondwera kwakukulu, nathamanga kukauza ophunzira ake. Koma pamene anali pa njira Yesu anakomana nawo nati, “Kondwerani!” Ndipo anadza namgwira Iye pa mapazi, namgwadira. Pomwepo anawauza, “Musaope. Pitani kauzeni abale anga kuti amuke ku Galileya ndipo adzandiona ine komweko.”

Asirikali aja amene analondera manda analowa m'mzinda napereka lipoti kwa ansembe akulu zimene zinachitika. Ansembe aja anakhala upo, napatsa asirikaliwo ndalama zambiri nati, "Kazinenani kuti ophunzira ake anadza usiku namuba Uja m'mene ife tinali m'tulo." Anawauzanso kuti, "Ngati ichi chidzamveka kwa Pilato, ife tidzamgwetsa mtima, ndipo tidza-kukhalitsani opanda nkhawa." Tsono asirikali aja analandira ndalamazo, nachita monga anawalangiza. Mbiriyo inabuka mwa Yerusalemu kufikira zaka zambiri, ngakhale mpaka lero.

Ophunzira khumi ndi mmodzi otsalawo anapita ku Galileya ku phiri limene Yesu anawauza kuti akawapeza. Pamene anamuona Yesu, onse anampembedza Iye, koma ena anakayika.

Tsono Yesu analankhula nawo nthawi yotsiriza nanena, "Pitani kwa anthu a mitundu yonse, mukawasandutse ophunzira anga, ndi kuwabatiza m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera; ndi kuwaphunzitsa kuti asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu. Ndipo ineyo ndili nanu masiku onse, kufikira kutha kwa dziko lino lapansi." Amen.

MAFUNSO

1. Kodi Yosefe wa ku Arimatea anafunsa Pilato chiyani?
2. Afarisi anaopa kuti zinthu zina zikhoza kuchitikira Yesu thupi lake pa tsiku la chitatu. Chifukwa chiyani?
3. Ndi ayani amene anapita kukaona Yesu pa tsiku loyamba? Nanga anapeza chiyani atafika ku manda?
4. Pambuyo pobwerera kwa ophunzira ake kukawauza iwo zimene anapeza, kodi azimayiwo anakomana ndi yani?
5. Yesu anawauza ophunzira ake kuti akomane naye ku malo ena kupatula Yerusalemu. Malo amenewo anali ati?
6. Pa phiri Yesu anali ndi lamulo lofunika kwambiri kupereka ophunzira ake. Yesani kunena mawu a Yesu osowa pano: "Pitani kwa anthu a mitundu yonse, mukawasandutse _____ anga, ndi kuwa_____ m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la _____; ndi kuwaphunzitsa kuti asunge zinthu zonse zimene ndinakulamu-lirani inu. Ndipo ineyo ndili nanu masiku onse, kufikira kutha kwa dziko lino lapansi."

ZOONA ZA UZIMU

1. Yesu ali ndi moyo lero. <u>Yesu sali munthu amene akhoza kuikidwa m'ndende ndi kumupha. Iye ndi Mulungu wa muyaya</u>. Iye alibe chiyambi ndi mapeto. Dongosolo lake la Mulungu pa chiyambi cha dziko linali kubwera pa dziko lapansi monga ngati munthu ndi kukhala mtumiki wozunzika. Chinali chifuniro chake kuti apachikidwe pa tsiku limenelo ndi mwa njira imeneyo. Madongosolo ake a Mulungu sangathe kulephera ndipo munthu wina aliyense sakanatha kupambana Iye m'pang'ono kapena kumtsitsa Iye. Iye akukhalabe Mulungu, ndipo nthawi zonse Iye yekhayo adzakhala Mulungu woona.
2. Afarisi anakhulupirira mawu ake a Yesu kwambiri kuti iwo anakhazika alonda olondera manda ake nthawi imene Iye atamwalira chifukwa analonjeza kuti adzaukanso. Iwo anakhulupirira mawu a asirikali atawauza cha chimene chinachitika; ngakhale kuwapatsa ndalama zambiri kuti anene bodza cha chimene chinachitika. Atsogoleri omwewo analipo pamene Yohane anabatiza Yesu. Anamva mawu amene Mulungu analankhula kuchokera kumwamba kutsimikizira kuti Yesu anali ndani. Anthu amenewo anali mboni pa zozizwitsa zimene Yesu anazichita. Komanso nthawi yina anakhwiya naye atachiritsa munthu wa dzanja lopuwala pa tsiku la Sabata. Anamuona Iye kuchotsa ziwanda zambiri kwa iwo amene anagwidwa nazo, ndipo anaona Iye kukhululukira anthu ambiri machimo awo. Afarisi aja anazindikira kuposa ena onse za moyo ndi uthenga wa Yesu, komabe sanakhulupirire chikondi chimene Mulungu anafuna kuwapatsa. Iwo sanalape machimo awo. Sanafune kupereka ndi kulamulidwa miyoyo yawo ku ulamuliro wa Yesu Khristu.

   <u>Kukhala ndi ubale ndi Yesu Khristu ndi koposa kungophunzira ndi kukhulupirira zoona za moyo wake. Nkupambana kukhala m'chipembedzo chatsopano kapena chosiyana. Yesu amafuna ife kuti tilape, kukhulupirira Iye ndi kumpereka Iye miyoyo yathu. Amafuna kuti akhale mbuye ndi mtsogoleri wa miyoyo yathu. Amafuna kuti alamulire ife ku nthawi iliyonse ya miyoyo yathu</u>.

3. Yesu ndi yani?
   -Yesu anabadwa kwa namwali.
   -Yesu anadzitchula kuti anali Mulungu.
   -Yesu anachita zozizwitsa zambiri nakhululukira anthu amene analapa machimo awo.
   -Yesu anafa pa mtanda kulipira dipo la machimo athu pamaso pa Mulungu wa chilungamo.
   -Yesu anaukanso kwa akufa ndipo ali ndi moyo lero.
   -Yesu akufuna inenso kuti ndilape machimo anga ndi kupereka moyo wanga kwa Iye.

Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti Yesu sanafe kuti akhale chitsanzo chabe. Koma anafa m'malo mwanu ndi mwanga…ife amene tiyenera kukhala pamaso pa Mulungu ndi kuweruzidwira zolakwa zathu zonse zimene tamchimwira Iye m'miyoyo yathu.

Mawu a Mulungu anena mu Aroma 10:13 kuti "...aliyense amene adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka."

*Izi zitanthauza kuti osalabadira zinthu zonse zanga zakale, ndikhoza kuitana Yesu kuti alowe m'moyo mwanga ndipo Iye adzandikhululukira ine machimo anga onse nakhala m'moyo mwanga.
*Zitanthauza kuti kuchokera mu nthawi imene Yesu alowa m'moyo mwanga, machimo anga onse: akale, amene ndichita tsopano, ndiponso akutsogolo; onsewo akhululukidwa pamaso pa Mulungu. Izi sichifukwa cha china chilichonse chimene ine ndachita ayi. Sichifukwa choti ndasankha chipembedzo chabwino ayi. Sichifukwa choti ndakhala munthu wangwiro ayi. Sichifukwa choti makolo anga ali a gulu lina lapadera ayi. Koma ndi pokhapo chifukwa chimodzi…makamaka kuti ndavomereza nsembe imene Yesu anachita pamene anatifera ife pa mtanda.
*Zitanthauza kuti kuchokera ku nthawi yomwe ino, ine ndili munthu wangwiro pamaso pa Mulungu, wopanda chifukwa. Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuti mphoto ya uchimo ndi imfa, koma imfa ya Yesu ndi yokwanira kundipangitsa ine kukhala wolengedwa watsopano ndikasankha kumtsatira Iye.

Ngati mukufuna kukhululukidwa ndi Mulungu tsopano lino m'moyo mwanu, ndipo mukafuna kukhala wotsatira wake wa Yesu, mungampemphe Iye kuti alowe m'moyo mwanu pompano. Simuyenera kukhala m'malo apadera a chipembedzo, kapena kunena mawu apadera kapena mawu atsenga. Koma chofunika ndi kubwera pamaso pa Mulungu ndi kuvomereza kukhulupirira kuti Yesu ndi Mulungu ndi kufuna kuti akhale mbuye ndi wolamulira wa moyo wanu.

Mungapemphere motere: "Atate, ndikudziwa kuti ndine wochimwa. Ndikukhulupirira kuti Yesu anafa pa mtanda naukanso kwa akufa kundipulumutsa ine ku machimo anga. Ndikulapa machimo anga. Ndikupatsani moyo wanga. Lowani m'moyo mwanga ndi khululukira machimo anga. Zikomo kwambiri chifukwa cha chikondi chanu kwa ine. M'dzina la Yesu, amen."

4. "<u>Ndipo Ineyo ndili nanu masiku onse, kufikira kutha kwa dziko lino lapansi</u>."

Mawu a Mulungu anena mu Yohane 14:2,3 kuti, "M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikunali kutero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli ineko, mukakhale inunso."

Yesu analonjeza kuti ALIYENSE amene apereka moyo wake kwa Iye adzakhala naye Kumwamba mpaka muyaya. Kumwamba ndi malo a Mulungu Atate. Ngati tavomereza Yesu m'moyo mwathu, tidzakhala naye Kumwamba mpaka muyaya. Izi zitanthauza kuti Yesu adzakhala nafe pano pa dziko lapansi, komanso tikamwalira tidzakhala nawo moyo wosatha ndi Iye Kumwamba.